

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

KODI MNANSI WANGA NDI NDANI?

Wachilamulo wina anadza kwa Yesu kudzamuyesa namufunsa kuti: “Ndichite chiyani kuti ndipeze moyo wosatha?” (Luka 10:25-37) Yesu anamuyankha nati, M'chilamulo mulembedwa chiyani? Wachilamuloyo anayankha nati kwa iye, “Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako yonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mnansi wako monga iwe mwini.” Yesu anayankha kuti, “Wayankha bwino; chita ichi, ndipo udzakhala ndi moyo.”

Koma pofuna kuti aoneke ngati wolungama ndi wabwino, wachilamuloyo anafunsa kuti, “Ndipo mnansi wanga ndani?”

Wachilamuloyo anali Myuda, ndipo atsogoleri achipembedzo achiyuda pa nthawiyo ankakhulupirira kuti Ayuda ena okha ndiwo amayenera kukhala anza. Kwa Ayuda, udindo wokhala mnansi sumafikira kwa akunja ndipo makamaka osati kwa Asamariya amene Ayuda amawaona ngati agalu ndiponso ngati ana a njoka. Ayuda ankadana kwambiri ndi Asamariya moti nthawi zina amayenda njira yaitali ndi yozungulira, mpaka kukaoloka mtsinje wa Yordani, mmalo mwa njira yachidule yodutsa mu Samariya; pofuna kupewa fuko lonyozekali.

Poganizira zimenezi, Yesu anafotokoza nkhani imene anthu ambiri masiku ano amaitchula kuti Msamariya Wachifundo.


Myuda wina ankachokera ku Yerusalemu kupita ku Yeriko pamene anakumana ndi achifwamba. Anamumenya, kumulanda zake zonse, namuvula zovala zake, nkumusiya ali thapsaa chigonere panjira. Wansembe, munthu wopatulidwa kuti agwire ntchito ya Mulungu, anaona munthu wopenyedwayo ndipo anamuthawa poyenda kutsidya lina la msewu. Kenako kunabwera Mlevi wina. Iye anayang'ana munthu wamagazi, wovulazidwa

uja, anamupima, nadutsanso mbali ina ya msewu. Msamariya wina, wonyansidwa ndi Ayuda, anayenda mumsewu womwewu. Pamene anaona Myudayo, ali wamaliseche ndi wokwapulidwa, anagwidwa chifundo.

Msamariyayo anatsuka, nasamalira ndi kumanga mabala a Myudayo. Anamukweza pa bulu wake nkupita naye kunyumba ya alendo. Anamulipira Myudayo malo ogona ndi chakudya, nasiya mau kuti azimusamalira. Msamariyayo anauza woyang'anira nyumba ya alendoyo kuti ngati ataonjezera zinthu zina, iye adzalipira akadzabweranso.

Yesu atamaliza fanizolo anafunsa kuti: “Uti wa awa atatu, uyesa iwe, anakhala mnansi wa iye uja adagwa m'manja a achifwamba?” Wachilamuloyo anayankha kuti, “Iye wakumchitira chifundo.” Yesu anamaliza ndi kumulangiza kuti: “Pita nuchite iwe momwemo.”

Pokhala ana a Mulungu, tonse tikuitanidwa kuti tikhale ndi mtima komanso maganizo okhala ngati a Msamariyayu. Mu chikhalidwe chimene Ayuda anali kusawalabadira ndi kuwasala Asamariya, anali Msamariya yemwe ankatumikira mwachikondi pa zosowa za Myuda. Nzochititsa chidwi kuona kuti Yesu sananenepo za Myuda amene anathandizapo Msamariya atavulazidwa. Sipayenera kukhala kusiyana kwa ana a Mulungu kaya anabadwira mgulu la onyozeka kapena onyozawo. Tiyenera kukhala okoma mtima ndi achikondi kwa aliyense amene timakumana naye mosasamala kanthu za fuko, malo ao mu fuko lao, mtundu, chipembedzo, mtundu wa khungu, kapena banja limene akuchokera. Uwu ndi umodzi mwa mizati ya moyo wachikhristu ndipo uyenera kumasiyanitsa anthu a Mulungu kuchokera kumadera ndi zikhalidwe zao zosiyanasiyana. ■



“Tiyenera kukhala okoma mtima ndi achikondi kwa aliyense amene timakumana naye mosasamala kanthu za fuko, malo ao mu fuko lao, mtundu, chipembedzo, mtundu wa khungu, kapena banja limene akuchokera.”

Kukongola kwa
kusiyana m'machitidwe
2
Mau a Mkonzi
3

Kuphunzira Baibulo:
Kufanana kwa
Akhristu (Kusalana)
4

Kufanana
kwachikhristu
motsutsana ndi
tsankho
5-6

Mafunso ndi
Mayankho: Ukwati
wa pakati pa anthu a
mitundu yosiyana
7

Kodi Mukudziwa?
Mau a Nyengo Yake
8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza


Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

KUKONGOLA KWA KUSIYANA M'MACHITIDWE

Pamene Mulungu anaona zonse zimene analenga anati, “zinali zabwino ndithu” (Genesis 1:31). Mitengo, zitsamba, maluwa, mbalame, zamoyo za m’nyanja ndi nyama zinali zosiyanasiyana komanso zamitundumitundu. Chilengedwe chenicheni chimanena za Mulungu amene amakonda mitundu yosiyanasiyana. Naonso anthu sikuti ali osiyana. Iye anatilenga tonsefe mwapadera, chifukwa palibe anthu awiri amene ali ofanana kotheratu.



Anthu ali ndi umunthu, makhaliidwe, mphamvu, ndi maonekedwe osiyanasiyana. Kuphatikiza pa kusiyana kwa anthu, pali mitundu ndi zikhaliidwe zosiyana komanso pali kusiyana pakati pa magulu ndi mitundu ya anthu yomwe inamwazikana padziko lonse lapansi. Kusiyanasiyanku sikukuyenera kuopedwa ndi ana a Mulungu koma tikulandire ngati chabwino. Ngakhale kuti anthu onse ndi ofanana

pamaso pa Mulungu, moyowu ndi wosangalatsa kwambiri chifukwa cha mitundu yosiyanasiyana. Akhristu ayenera kuyamikira chilengedwe chokongola cha Mulungu cha anthu osiyanasiyana.

Palibe cholakwika kuti anthu amitundu yosiyanasiyana azilemekeza komanso kuyamikira chikhaliidwe chawo pokhapokha ngati potero sakunyozza zikhaliidwe ndi mafuko a ena. Molakwika dzikoli limalimbikitsa kukhalira pamodzi kwa zikhaliidwe zosiyanasiyana ndi malingaliro akuti ndi zochokera kwa anthu osati kwa Mulungu. Akhristu akhoza kukonda ndi kusangalala chifukwa cha mitundu ndi zikhaliidwe zosiyanasiyana popanda kukodwa mu mchitidwe wakuti choipa kapena chabwino zimatengera ndi mmene munthu akuonera zinthu ndipo izi nthawi zambiri zimalumikizana ndi kukhalira pamodzi kwa zikhaliidwe zamitundu yosiyanasiyana.

Zikhaliidwe za anthu zikuyenera kuyamikiridwa pomvetsetsa kuti zikhulupiriro zonse ndi zikhaliidwe sizili zofanana. Uthenga wabwino sunalalikidwe kuti uwononge zikhaliidwe; koma pamene miyambo ina yochitika mmenemo ikusemphana ndi Mau a Mulungu, anthu akuyenera kuzisiya zoipazo ndi kulola kuti choonadi cha Mulungu chikhale pamwamba pa zonse. Pali kukongola mu kusiyana kwa mitundu ya anthu pamene zones ziikidwa pamodzi ndi chilungamo cha Mulungu. ■

“Mulungu afulumize nthawi imene tsankho la fuko lonse lidzathe ndipo mzimu uliwonse umene Khristu anaufera uzindikiridwe kuti uli wantengo wapatali pamaso pake.”

—FG Smith (Mtumiki Woyamba wa mpingo wa Church of God, 1901)

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m’dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Chifukwa chake zinthu ziri zonse mukafuna kuti anthu achitire inu, inunso muwachitire iwo zotero. —Mateyu 7:12

Dziko lathu likanakhala malo abwinoko ngati anthu akanatsatira mfundo iyi yosavuta kukhala lamulo la moyo wathu: Chitirani aliyense mmene mukufuna kuti akuchitireni. Nyuzi masiku ano zadzaza ndi nkhani za kusalana, maudani, kusakhululuka, kusankhana mitundu, tsankho, ndi mikangano. Ndine woyamikira kwambiri kuti Yesu Khristu pamwamba pophunzitsa njira yabwino yakuti titsatire amaperekanso chisomo ndi chikondi chaumulungu kwa anthu ochokera ku mafuko ndi zikhalidwe zosiyanasiyana zomwe zingapangitse kuti onse akhoza kukhala pamtendere ndi mogwirizana.

Mutu wa nkhani mu kalata ya ulendo uno ya Choonadi cha Uthenga Wabwino ndiwo “Kufanana kwa Chikhristu.” Mulungu anatilenga tonsefe mofanana, ndipo ngakhale kuti tili ndi zinthu zosiyanasiyana monga zilankhulo, kochokera, mtundu wa khungu ndi zina zotero, ife monga Akhristu tiyenera kukonda aliyense ndi kulemekeza aliyense.

Pamene ndimasinkhasinkha za mutu umenewu, ndinalingalira zokhala ndi olemba ena ochokera m'maiko ndi mafuko osiyanasiyana. Mu dziko lililonse, pali nkhani za tsankho kaya kuchokera ku kusankhana mitundu, kusalana, kusiyantsa pakati pa anthu malingana ndi kupeza kwao ndi zina zotero. Tonsefe titha kuphunzira kuchokera kwa wina ndi mnzake ndipo pali phindu lalikulu pa kugawana ndi ena. Komabe, Ambuye ananditsogolera kuti ndifike pa mfundo iyi: Tonse tili ndi maganizo, malingaliro ndi nkhani yakuti tinene, koma muyezo wa choonadi sutengera pa nkhani yanga kapena nkhani yanu. Mau a Mulungu ndiwo muyezo wa choonadi umene tiyenera kuyezera chilichonse, posawerengera maganizo ndi malingaliro athu. Ndi nkhani yomvetsa chisoni pamene Mkhristu akusamala kwambiri nadzipereka ku fuko ndi chikhalidwe chake kusiyana ndi chikhulupiriro chake mwa Khristu.

Anthu ambiri amakhala ndi malire posankha zikhalidwe ndi machitidwe ao potengera zomwe anakumana nazo pa magawo onse okhudza mutuwu. Ambuye tithandizeni kuyang'ana mu galasi la Mau a Mulungu ndi kudzifufuza miyoyo yathu. Anthu onse sachitiridwa mofanana ndi mwaulemu chifukwa cha uchimo. Pali kusiyantsa, kusankhana mitundu, kusankhana ndi kusalana chifukwa cha chuma, mtundu wa khungu, fuko, ndi malo a munthu mufuko lao. Izizi zimachitika ku North ndi South America, Europe, Asia, ndi ku Africa. Posatengera kanthu za kusalana kumene kuli pakati pathu, Akhristu ayenera kukonda ndi kulemekeza anthu onse. Sitiyenera kubweretsa tsankho ndi mkwiyo pakati pa anthu mu mpingo wa Mulungu; tiyenera kusachita nao izi mwa chisomo cha Mulungu. Kusowa chilungamo ndi zopweteka zonse zikuyenera kuperekedwa kwa Yehova.

Kuli kulakwa pamene tiweruza kapena kuzunza munthu chifukwa cha mtundu wa khungu, kaya ndi lakuda, loderapo kapena loyera. Ngakhale sizivuta kuvomereza kuti munthu wolemera sayenera kusala munthu wosauka ndiponso kuti fuko limene lili ndi mphamvu lisanyoze fuko lomwe lili lofooka. Komabe, kuli kofunika ndithu kuti munthu wosauka asasale munthu wolemera ndi kuti fuko lofooka asachite mokondera potsutsana ndi fuko lomwe lili lamphamvu kwambiri pazandale.

Ngakhale kuti zomwe zandichitikira zili zosiyana ndi zanu, ndakhala ndikuganiziridwa molakwika, kuzunzidwa, kutchulidwa maina ndi kunamizidwa chifukwa cha mtundu wa khungu langa kuyambira kwathu ngakhalenso kumaiko akunja. Anandichitira izi ndi anthu amene amati ndi Akhristu komanso anthu ochimwa a m'dzikoli. China chake chikadzuka mkati mwanga kuti ndibwezere chifukwa cha chisalungamocho, Mulungu amandithandiza kuti ndiyenera kukhululukira ndi kusakhala woipidwa. Umenewo ndiwo muyezo wa Baibulo!

Ifeyo pokhala oyera mtima sitiyenera kudziyesa tokha ndi muyezo wa dziko lapansi, koma tikuyenera kusamalira aliyense mwachikondi komanso kukhululukira iwo amene atilakwira ife. Mulungu athandize anthu ake kukhala pamodzi mu umodzi.

Michael W. Smith

October 2023



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Kufanana kwachikristu (Kusalana)

Kuwerenga Malemba: Pakuti inu nonse muli ana a Mulungu, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu. Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khristu mudavala Khristu. Muno mulibe Myuda, kapena Mgriki, muno mulibe kapolo, kapena mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi; pakuti muli nonse mmodzi mwa Khristu Yesu. —Agalatiya 3:26-28

Tanthauzo: Malingana ndi (Vocabulary.com) kusalana kumatanthauza kusiyantsa pakati pa anthu awiri kapena opitirirapo kapenanso zinthu ziwiri kapena zopitirirapo. Komabe, kawirikawiri amagwiritsidwa ntchito pofuna kunena za kuchitiridwa zinthu mopanda chilungamo kapena mwatsankho kwa gulu limodzi la anthu pamwamba pa gulu lina.

Mwachidule: Anthu onse analengedwa ndi Mulungu ndipo ali ofanana pamaso pake. Uthenga Wabwino unali wopita kwa anthu a chinenero chilichonse, mtundu uliwonse, fuko lililonse, dziko lililonse, ndiponso mmene alili pachuma. Akhristu ayenera kukhala mu umodzi ndi kukonda wina aliyense, nakhala pamwamba pa kusalana, kusakhululuka, ndi tsankho zimene zimapezeka mdzikoli.

I. Wolengedwa ndi Mulungu

- A. Genesis 1:27 Mulungu analenga anthu m'chifanizo chake.
- B. Malaki 2:10 Onse ali ndi Atate mmodzi.
- C. Machitidwe a Atumwi 17:26 Mitundu yonse inachokera ku mtundu umodzi.
- D. Miyambo 22:2 Yehova analenga wolemera ndi wosauka omwe.

II. Uthenga Wabwino wapadziko Lonse

- A. Yohane 3:16 Mulungu amakonda aliyense.
- B. Agalatiya 3:26-28 Onse ali ana a Mulungu.
- C. Chivumbulutso 14:6 Uthenga wabwino ulalikidwa kwa mitundu yonse.
- D. Chivumbulutso 5:9-10 Anthu ochokera m'mitundu yonse aomboledwa.
- E. Aroma 10:12 Palibe kusiyana pakati pa Myuda ndi Wamitundu ina.

III. Iye sakondera posankha

- A. Machitidwe 10:34-35 Mulungu alibe tsankho. (Onaninso Aroma 2:11).
- B. Yakobo 2:1-10 Kusalana ndi kusankhana ndi uchimo.

IV. Khoma lapakati lolekanitsa

- A. Aefeso 2:11-19 Chotchinga pakati pa Ayuda ndi Amitundu chinasweka. Onse ndi nzika zinzathu.
- B. Machitidwe a Atumwi 10:28 Palibe munthu amene ayenera kutchedwa wosafunikira.
- C. 1 Akorinto 12:25 Pasakhale magawano m'thupi.

V. Mmodzi mwa Khristu

- A. 1 Akorinto 10:17 Mkaté umodzi ndi thupi limodzi.
- B. 1 Akorinto 12:12-13 Ziwalo ndi mafuko ambiri koma thupi limodzi.
- C. Aroma 12:5 Ziwalo za wina ndi mzake.

VI. Umodzi

- A. Yohane 17:20-22 Yesu apempherera umodzi.
- B. Salmo 133:1-3 Khalani pamodzi mu umodzi!
- C. (Afilipi 2:3-5) Lemekezani ena kuposa inu eni.

VII. Kondani monga abale

- A. Yohane 13:34-35 Lamulo lokondana wina ndi mnzake.
- B. 1 Atesalonika 3:12-13 Muonjezere ndi kuchuluka m'chikondi.
- C. 1 Petro 1:22 Kondanani wina ndi mnzake ndi mtima woyera.
- D. 1 Petro 3:8-9 Khalani ndi chifundo; kondani monga abale.
- E. 1 Yohane 3:14-18 Iye wosakonda mbale wake akhala mu imfa.

VIII. Chiweruzo cholungama

- A. Levitiko 19:15 Wosauka kapena wamphamvu, weruzani mwachilungamo.
- B. Yohane 7:24 Musaweruze monga mwa maonekedwe.

IX. Yankho laumwini pa tsankho

- A. Marko 11:25-26 Khululukirani zolakwa za anthu.
- B. 1 Atesalonika 5:15 Musabwezere choipa pa choipa.
- C. Mateyu 5:43-44 Kondani, pempherani, chitani zabwino.
- D. Ahebri 12:14-15 Chenjerani ndi muzu wa zowawa.

X. Osati a dziko lino

- A. Yohane 17:15-17 Okhala m'dziko lapansi, koma osati a dziko lapansi.
- B. Aroma 12:2 Musafanizidwe ndi makhalidwe a panso pano;

Kumaliza

Musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemero wopanda pake; koma m'kudzichepetsa mtima yense ayese mnzake omposa iye mwini. Aliyense asapenyere zake za iye yekha, koma yense apenyereenso za mnzake. Lolani mtima uwu ukhale mwa inu, umene unalinso mwa Khristu Yesu. —Afilipi 2:3-5

KUFANANA KWACHIKHRISTU MOTSUTSANA IDI TSANKHO

Ziphunzitso za Yesu Khristu zimaposa miyambo ndi zikhalidwe za m'badwo uno. M'dziko limene maudani, mikangano, kusalana, ndi tsankho zachuluka kuyambira pa chiyambi cha nthawi, pali kuitana kwamphamvu ndi komasula ndi kumene kumakumana ndi chikondi, chifundo, chikhululukiro komanso kufanana.



“Akhristu sayenera kukhala atsankho kapena kukondera koma ayenera kukonda ndi kulemekeza anthu onse.”

Wolengedwa ndi Mulungu

Ngakhale kuti pali kusiyana kwa mitundu, mafuko, maiko, zinenero, mtundu wa khungu, ndi chikhalidwe cha chikhalidwe cha anthu, tonsefe ndife zolengedwa za Mulungu ndipo ndife ofanana pamaso pake. “Mulungu adalenga munthu m'chifanizo chake ... adalenga iwo mwamuna ndi mkazi” (Genesis 1:27). Chifukwa cha uchimo, pakhala pali anthu padziko lonse lapansi a m'badwo uliwonse amene amazunza anthu ndi magulu a anthu chifukwa cha kusiyana maganizo. Ndithudi, ife tonse tili ndi tate mmodzi, ndipo ndi Mulungu amene “anapanga ndi mwazi umodzi mitundu yonse ya anthu, kuti akhale ponse pa nkhope ya dziko lapansi” (Machitidwe 17:26). Ngakhale kuti banja laumunthu limasiyana osati m'kaonekedwe kakunja kokha komanso mu umunthu, miyambo, malamulo, ndi miyambo, anthu onse amachokera ku chiyambi chimodzi. Monga momwe Miyambo 22:2 imanenera kuti: “Wolemera ndi wosauka amakomana pamodzi: Yehova ndiye amene anawapanga onse.” Tonse ndife abale ndi alongo ndipo tiyenera kulemekezana ndi kukhalira limodzi muumodzi ndi m'chigwirizano.

Uthenga Wabwino wapadziko lonse

Uthenga wa chipulumutso uli wa chiyembekezo ndipo ndi wa kwa anthu onse. “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi” (Yohane 3:16). Chikondi chachikulu cha Mulungu chimakhudza anthu a mtundu uliwonse, ndipo Yesu anafera anthu onse. Mtumwi Yohane analankhula za mngelo amene analalikira uthenga wabwino wosatha kwa “iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uliwonse ndi fuko ndi manenedwe ndi anthu” (Chivumbulutso 14:6). Iye analalikira uthenga wabwino wamuyaya kwa iwo akukhala padziko lapansi. Paulo

analemba kuti: “Pakuti inu nonse muli ana a Mulungu, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu...Muno mulibe Myuda, kapena Mgriki, muno mulibe kapolo, kapena mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi; pakuti muli nonse mmodzi mwa Khristu Yesu” (Agalatiya 3:26-28).

Iye sakondera posankha

Petro, amene anakadziwa bwino za kusiyana kumene kunalipo pakati pa Ayuda ndi Amitundu ina, analankhula za choonadi chosatha. “Zoono ndizindikira kuti Mulungu alibe tsankho; koma m'mitundu yonse, wakumuopa Iye ndi wakuchita chilungamo alandiridwa naye” (Machitidwe 10:34-35). Paulo akulankhula choonadi chomwecho mu Aroma 2:11, “Pakuti palibe tsankho kwa Mulungu.” Mulungu amakonda anthu onse ndipo sasankha wina aliyense. Iye alibe tsankho ndipo sakondera munthu wina chifukwa cha chuma chake, kutchuka kwake, mtundu wa khungu, chinenero, kapena banja. Inde, Akhristu ayenera kukhala ndi mzimu komanso maganizo ofanana ndi anthu amene ali osiyana ndi iwo eni. Buku la Yakobo pa mutu wachiwiri akufotokoza momveka bwino za nkhani imeneyi. Ngati munthu wolemera ndi wosauka alowa mu msonkhano, ndipo munthu wolemerayo asonyezedwa ulemu wapadera, kodi kumeneko sikukondera? “Ngati muli ndi tsankho, muchita tchimo” (Yakobo 2:1-10). Ichi ndi chiphunzitso chomveka bwino ndipo chimagwira ntchito kwa Akhristu onse masiku ano. Choonadi cha Mau a Mulungu chikuyenera kugwiritsiridwa ntchito pamene pali kusalana, tsankho, kusankhana mitundu, kupatulana ndi kuikana m'magulu pakati pa anthu, ndi tsankho la mtundu uliwonse. Mzimu wovomereza ndi wa kukoma mtima ukuyenera kuonekera mwa Akhristu a fuko

(Yapitirira pa tsamba 6)

lililonse, mtundu aliwonse, ndi gawo la anthu uliwonse. Akhristu sayenera kukhala atsankho kapena kukondera koma ayenera kukonda ndi kulemekeza anthu onse.

Khoma lapakati losiyantsa

Kupyolera mu mwazi wa Khristu, khoma lapakati losiyantsa Ayuda ndi Amitundu ina lagwetsedwa. Khristu wayanjanitsa “awiriwa ndi Mulungu, m’thupi limodzi mwa mtandawo, atapha nao udaniwo....Pamenepo ndipo simulinsolo alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyera mtima ndi a banja la Mulungu” (Aefeso 2:11-19). Sipayenera kukhala magawano kapena kusankhana m’banja la Mulungu, koma onse ayenera kusamalirana wina ndi mnzake (1 Akorinto 12:25). Pali



anthu amene amakhala ndi maudani ndi anzawo chifukwa cha fuko lao kapena mtundu wa khungu lao ndipo amawaona enawo ngati otsika. Ayuda ankawaona Amitundu ina ngati otsika, koma Petro anachitira umboni pa Machitidwe 10:28 kuti: “Mulungu anandionetsera ine ndisanenere aliyense ali munthu wamba kapena wonyansa.” Nkulakwa kuona mtundu wa anthu kukhala wosafunika kapena wosafunika, chifukwa onse ndi ofanana.

“Mtanda ndi wovuta kupirira pa kusolidwa, koma palibe malo oti woyera mtima akhale ndi chakukhosi kapena kusakhululuka kupirira kusolidwa, koma palibe malo oti woyera mtima azisungira chakukhosi kapena kusakhululuka.”

Mmodzi mwa Khristu

Ngakhale kuti dziko likhoza kusiyantsa ndi kugawanitsa, Malemba amaphunzitsa kuti pakati pa anthu a Mulungu pakuyenera kukhala umodzi. “Chomwecho ife, ndife ambiri, tili thupi limodzi mwa Khristu, ndi ziwalo zinzake, wina ndi wina” (Aroma 12:5). “Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse tinabatizidwa kulowa m’thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Agriki, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu

mmodzi” (1 Akorinto 12:13). Kutipakhalira umodzi pamalo pamene pali kusiyana kwachibadwidwe, tikuyenera kukhala ndi maganizo a Khristu komanso kutsatira mau a chilimbikitso opezeka pa Afilipi 2:3 akuti, “musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pake, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzake omposa iye mwini.”

Kondani monga abale

Mosawerengera za kusiyana kulikonse, Akhristu akulamulidwa ndi Khristu kuti, “Mukondane wina ndi mnzake” (Yohane 13:34). Chilichonse chochepera apa ndi uchimo, chifukwa “Iye amene sakonda akhala muimfa” (1 Yohane 3:14). Petro anaphunzitsa kuti tikhale, “ochitirana chifundo, okondana ndi abale... odzichepetsa” (1 Petro 3:8-9). Chikondi chochokera

kwa Mulungu chimagwetsa mchitidwe wosalana, kusankhana, kupatulana pakati pa anthu, kusiyana mitundu, tsankho, ndi zina zotero. Chikondi chenicheni chimasintha mmene timaonera ndi kuchitira ndi anthu ena. Mkhristu amene ali ndi chikondi cha Mulungu amalemekeza ndi kuchitira ulemu anthu onse.

Chiweruzo cholungama


Ziweruzo ziyenera kuperekedwa m’moyo, koma zisakhale zoyang’ana pa fuko kapena chuma. Malamulo a Mose amanena kuti: “Musamachita chisalungamo pakuweruza mlandu (Levitiko 19:15). Khristu mwini anaphunzitsa kuti, “Musaweruze monga maonekedwe, koma weruzani chiweruzo cholungama” (Yohane 7:24). Tiyeni tiziweruza molingana ndi choonadi osati molingana ndi zifukwa zimene tili nazo kale ndiponso kusankhana.

Yankho laumwini pa tsankho

Ndi zomvetisa chisoni kuti anthu ena nthawi zonse sachitira ena zinthu mofanana, mwachikondi, ndiponso mwaulemu zimene Baibulo limaphunzitsa. Akhristu ayenera kutsatira zimene Baibulo limaphunzitsa mosasamala kanthu za zimene zikuchitika m’dzikoli. Mau a Mulungu amafotokoza mmene Mkhristu angachitire pamene akumana ndi nyengo imene wachitidwa mopanda chilungamo ndiponso wasalidwa. Yesu anaphunzitsa mwachindunji kuti tizikhululukira anthu amene atilakwira. “Mukupanda inu kukhululukira anzanu, Atate anunso wa Kumwamba sadzakhululukira inu machimo anu” (Marko 11:25-26). Mtanda ndi wovuta kupirira pa kusolidwa, koma palibe malo oti woyera mtima akhale ndi chakukhosi kapena kusakhululuka. “Penyani kuti wina asabwezere choipa womchitira choipa” (1 Atesalonika 5:15). M’malo mobwezera, Yesu analangiza kuti: “Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu” (Mateyu 5:43-44). Monga momwe pali tsankho lambiri, palinso kusakhululukira kuchulukira. Mkhristu ayenera kusamala pamene akuchitiridwa nkhanza, “kuti ungapuke muzu wina wa kuwawa mtima ungavute inu, ndipo aunyinji angadetsedwe nao” (Ahebri 12:14-15). Monga momwe khalidwe la tsankho lafalikira ku mibadwomibadwo, momwemonso uchitira mkwiyo. Sitingathe kukalowa Kumwamba ndi ichi kapena chinzake.

Osati a dziko lino

Yesu anapempherera kuti Mulungu ateteze ophunzira ake ku zoipa za dziko lapansi (Yohane 17:15). Zoipa zachuluka mudziko lathu; ndipo pali kugawana kwambiri m’maiko osiyanasiyana pa mafuko, chipembedzo, mtundu wa khungu, kapezedwe ka chuma ndi zina zotero. Ana a Mulungu akuyenera kukhala pamwamba pa mikangano ndi zinthu zakuthupi ngati izi, ndipo sizikuyenera kulowetsedwa mu mpingo wa Mulungu. Oyera mtima sayenera “kusanzidwa ndi makhalidwe a panso pano” (Aroma 12:2), kapena kudziwika ngati a dziko ndi zoipa zake. Iwo ayenera kupereka zitsanzo za chikondi, ulemu, kulemekezana, kukhululukira, ndi kuvomerezedwa ndi anthu onse. Palibe malo a tsankho kapena mkwiyo. Mulungu athandize Mkhristu aliyense kusiya maganizo a thupi la dziko lapansi ndi kuyenda mu chiyero. Njira ya kusasiyana ndi kuvomerezana ili yoona, yolondola, komanso yokongola. ■



Kodi Baibulo limaphunzitsa chiyani za maukwati a anthu osiyana mitundu?

Lamulo la Chipangano Chakale limaletsa ana a Israele kukwatira mzika za dziko la Kanani (Eksodo 34:14-16). Mulungu anauza Aisraele kuti aononge anthu a m'dzikoli komanso kuti asakwatirane nao. Mulungu ananena chifukwa chimene anaperekera langizoli, ndipo sichinali chokhudzana ndi mtundu kapena kaonekedwe ka khungu. “Ndipo musakwatitsane nao... Popeza adzapatutsa mwana wanu aleke kunditsata Ine, kuti atumikire milungu ina” (Deuteronomo 7:1-4). Mulungu ankafuna kuti anthu ake akhale oyera komanso osadetsedwa, ndipo azimulambira iye yekha basi.

Pamene Aisraele anayamba kukwatirana ndi mitundu ina ndi mafuko ena posamvera Mulungu, iwo amachita izi potengera moyo wopembedza mafano ndi kulambira milungu yosema zimene amachita achikunja. Aneneri anafuula motsutsana ndi mchitidwe umenewu (Malaki 2:11; Ezra 9:1-2). Chifukwa chakuti anasakanikirana ndi anthu a m'dzikolo, mitima yao idachoka pamaso pa Mulungu. Mfumu Solomo ndi chitsanzo chomvetsa chisoni cha zimenezi. “Ndipo mfumu Solomoni anakonda akazi ambiri achilendo, pamodzi ndi mwana wamkazi wa Farao, akazi a ku Mowabu, ndi a ku Amoni, ndi a ku Edomu, ndi a ku Sidoni, ndi Ahiti...Yehova adanena ndi ana a Israele za iwo, kuti, Inu musakalowa kwa iwo, ndipo iwo asadalowe kwa inu; zedi adzatembenusa mitima yanu kutsata milungu yao...Ndipo kunali, atakalamba Solomoni, akazi ake anapambutsa mtima wake atsate milungu ina” (1 Mafumu 11:1-5).

Lamulo loletsa kukwatirana pakati pa Aisraele ndi amitundu ina silinali lokhudzana makamaka ndi mtunduwo paokha koma kuti amitudu inayo akadawakopa iwo kuti azipembedza mafano. Chipangano Chatsopano chimaphunzitsa mfundo yofanana ndi imeneyi yokhudzana ndi ukwati. “Musakhale omangidwa m'goli ndi osakhulupirira osiyana; pakuti chilungamo chigawana bwanji ndi chosalungama? Kapena kuunika kuyanjana bwanji ndi mdima? Ndipo Khristu avomerezana bwanji ndi Beliyali? Kapena wokhulupirira ali nalo gawo lanji pamodzi ndi wosakhulupirira?” (2 Akorinto 6:14-15). Ukwati ndi goli lapafupi kwambiri pa maubale onse a anthu, ndipo Chipangano Chatsopano chimaphunzitsa kuti wokhulupirira sayenera

kukwatirana ndi wosakhulupirira; ndipo iyi si nkhani ya fuko kapena mtundu wa khungu.

Mose anakwatira Mmidiyani ndipo kenako anakwatira Mkusi. Miriamu ndi Aroni anamtsutsa Mose chifukwa cha ukwati wake. Mulungu anawakwiwira awiriwo, osati Mose, ndipo Miriamu anakhala wakhate (Nume 12:1, 9-10). Kutsutsa kwao kunali kokhudzana kwambiri ndi mphamvu ndi chikoka chao kuposa ukwati weniweniwo. Wothirira ndemanga pa Baibulo Albert Barnes analemba motere:

Kukwatiwa kwa Mose ndi mkazi wochokera ku fuko la Hamu sikunali koletsedwa, pokhapokha ngati iye sanali wa fuko la Kanani; koma panthawi iliyonse chikanakhala chonyansa ku mtundu oopsawo umene unkadziwika ndi Ayuda. Akhristu oyamba aja anaona kuti mu ukwati wa Mose ndi Mmidiyani kenako ndi Mkusi muli chithunzithunzi cha zochitika mtsogolomo chokhudza pangano ndi malonjezo a Mulungu kwa amitundu ina.

Mu Chipangano Chatsopano, pamene tikadali ndi mitundu yosiyanasiyana, “Pakuti kulibe kusiyana Myuda ndi Mgriki; pakuti Yemweyo ali Ambuye wa onse, nawachitira zolembera onse amene aitana pa Iye” (Aroma 10:12). Rute ndi Rahabu akuphatikizidwa mumzere wa makolo a Khristu. Zoonadi, Mulungu “ndi mmodzi analenga mitundu yonse ya anthu” (Machitidwe 17:26). Chipangano Chatsopano sichimaletsa kukwatirana pakati pa mitundu yosiyana.

Ukwati ndi chinthu chovuta kwambiri ndipo pali zinthu zambiri zofunika kuzilingalira. Ukwati uyenera kulowedwa ndi pemphero ndi uphungu wochulukira. Chikhulupiriro mwa Khristu, osati fuko kapena mtundu wa khungu, ndiwo muyezo wa Baibulo posankha wokwatirana naye. Komabe, nkhani zokhudza mafuko, miyambo, chikhalidwe, kusiyantsa anthu a mtundu umodzi, mtundu, mbiri ya kumene munthu akuchochera ndi zina zotero ziyenera kuganiziridwa mwapemphero malinga ndi chikhalidwe cha munthu. Maubale okhudza banja, zopsinja zochokera kwa otizungulira, ndi kuvomereza ana amene abwere mtsogolo ziyenera kuganiziridwa. Mu zikhalidwe zina, pali mavuto aakulu amene angayambitsidwe ndi ukwati wa anthu amafuko osiyanasiyana ndipo izi zingapangitse ukwatiwo kukhala wovuta kwambiri. Zolingalirazi sikuti ndi nkhani za uchimo koma zofunika nzeru ndi kumvetsetsana; ndipo zimasiyana malingana ndi malo komanso mmene ilili nkhaniyo. ■



KODI MUKUDZIWA?

“Kusankhana kwafalikira komanso kukuipiraipira padziko lonse lapansi, malinga ndi zotsatira za kafukufuku wa World Justice Project Maiko 70 pa 100 alionse aona tsankho likuipiraipira pakati pa 2021 ndi 2022. Kuyambira mu 2015, tsankho laonjezeka m’maiko atatu mwa anai amene bungwe la WJP linapangitsa.”

(2023, March 21). Tsankho Likuipiraipira Padziko Lonse . www.worldjusticeproject.org.



Mau a
Nyengo
Yake

KUDZIWIKA MWA KHRISTU

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu amwini wake. —1 Petro 2:9

Aisraele anali anthu osankhidwa kapena osankhidwa ndipo anali anthu apadera kwa Mulungu kuposa anthu ena onse. Anapatulidwa ndi mitundu ina kuti azilambira Mulungu yekha. Chinali chifuniro cha Mulungu kuti iwo asungebe umunthu wao ndi kusaipitsidwa ndi kulambira mafano kwa mitundu ina. Mulungu ankafuna kuti iwo asunge ndi kuteteza cholowa chao zivute zitani. Ayuda ankadziwika kuti anali anthu osankhika ake a Mulungu.

Yesu Khristu anabwera ndi kutiyanjanitsa ife tonse ndi Mulungu kudzera mu mwazi wake. Tikalandira chikhululukiro cha Mulungu ndi kupulumutsidwa ku mphamvu ya uchimo, timakhala zolengedwa zatsopano. Tili ndi chizindikiritso chodabwitsa, chatsopano mwa Yesu Khristu monga nzika za ufumu wa Mulungu. Tasankhidwa ndipo ndife ansembe achifumu.



CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Anthu adziko lapansi amafunafuna “kudziwika”. Pali ena atsankho komanso anthu omwe amakondera anza. Anthu akakhala ndi mtima umenewo, nthawi zambiri zimakhala chifukwa chakuti iwowo alibe mtendere weniweni. Kaya ndi chidani, kusadzidalira, kudzikonda, kunyada, umbombo, nkhani zabodza, kapena kusadziwa, komatu munthu akamanyoza mnzake, amavumbula umunthu umene wamangidwa pa maziko olakwika.

Ngakhale kuti tonse tili ndi cholowa chapadziko lapansi ndi fuko, umunthu wathu woyamba uyenera kupezeka mwa Mulungu komanso kuti ndife ana ake, chifukwa mmenemo muli mpumulo oona. Ambiri amavutika ndi zomwe iwo ali komanso momwe amaonekera. Yehova amafuna kuti tivomereze mmene anatilengera ndi kukhala pa mtendere. Tasankhidwa ndi Mulungu ndipo sityenera kulimbana ndi nkhani zopanda pake zomwe zili mdera lathu. Ndi kudziwika kwathu mwa Khristu komwe kudzatinyamule mpaka muyaya! ■